# SHERASONGWE PRIMARY SCHOOL

**2026 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION**

# CHICHEWA

**(Malikisi 100)**

**Dzina lanu:** ______________________________________________

**Dzina la sukulu yanu:** ______________________________________________

## Malangizo:

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi Masamba khumi ndi awili.
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi. **Gawo A, B, C** ndi **D**.
3. Lembani dzina lanu ndi dzina la sukulu yanu pamwamba pa tsambalino.
4. Lembani chimangirizo Kapena kalata mu Gawo **A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D**.
5. Yankhani mafunso a mu **Gawo B** ndi **C**m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse.
6. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozunguliza limbo lokhonza pafunso lililonse.
7. Muchitebulo chili pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi Lomwe lili kutsogolo kwake.
8. Pelekani kwa oyang'anila kulemba mayeso (invijileta) pepala lonseli nthawi ikakwana.

| **Funso** | **Chongani Zomwe mwayankha** | **Munomusale mbemo** | |
|---|---|---|---|
| **1** | | | |
| **2** | | | |
| **3** | | | |
| **4** | | | |
| **5** | | | |
| **6 – 45** | | | |
| | | | |

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**Gawo A:** (Malikisi 30)

Langizo: Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri alim'musiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena wa kalata. Mawu a chimangirizo kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu; **"MUDZI WA CHITSANZO**. Mwazina tsatani izi polemba chimangirizo chanu.

**Ndime yoyamba**

- Dzina la mudziwo.
- Komwe mudziwo ukupezeka
- Chiwerengero cha maanja a m'mudzimo.

**Ndime yachiwiri**

- Zomwe zikuchititsa kuti mudziwo ukhale wachitsanzo mderalo.
- Mabungwe omwe akuthandizira kuti mudziwo ufike pomwe wafikapo

**Ndime yachitatu**

- Phindu lomwe mudziwo wapeza pokhala wa chitsanzo.

**KAPENA**

**2.** Lembani kalata kwa azakhali anu omwe amakhala kutali ndi inu yowafotokozera za mnzanu wapamtima yemwe mwapeza. Mwa zina tsatani izi polemba kalata yanu.

**Ndime yoyamba**

- Cholinga cha kalata yanu
- Dzina la mnzanuyo
- Maonekedwe a mnzanuyo

**Ndime yachiwiri**

- Zomwe iye amakonda kuchita
- Zomwe mukuchita pofuna kulimbikitsa ubwenzi wanu

**Ndime yachitatu**

- Ubwino womwe mwawona pokhala ndi mzanu wapamtimayo

Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

EXAMINATION NO.:______________________________

Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

EXAMINATION NO.:______________________________

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## Gawo B (Malikisi 20)
## Kumvetsa nkhani

**3.** *Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawa.*

Mudzi utatha kumanda, mdzukulu m'modzi adapita kukauza a mfumu Lipote kuti mwambo wamaliro uyambe. Amfumu ataona kutha kwa mudziwo, mosakhalitsa adzukulu adatulukira atandondozana ngati midzodzo chithatha chili mmanja apa nkuti wotsogolera mwambo atauzanso anamalira ndi anthu onse zoyamba mwambowu. Atatero anthu angapo adatulutsa mfumu kukonzekera kupita kunsamba mfumu.

Wotsogolera mwambo adaimiria nayamba kuyakhula motere: "Pepani anamalira nonse, pepani gogo chalo. Tchaya, pepani amfumu lipote ndi mafumu onse, pepani amayi ndi abambo, anyamata ndi atsikana.

Tsopano tikufuna tiyambe mwambo wa maliro. Chonde tiyeni tikhale chete kuti tipereke ulemu woyenera pa maliro pano komanso kuti timvane. Tidziwa maliro alibe chizolowezi nanga tingatani poti ndi m'mene kunalembedwera motero, pepani pepani anamalira nonse tiugwire mtima wathu. Posunga nthawi tipemphe oyakhula onse kuti ayankhule mwachidule. Poyamba tipemphe akuchikadzi, akuchimuna kenako amfumu a m'mudzi uno kuti atiyakhule.

Ulemu kwa gogo Chalo Tchaya, Ulemu kwa nonse mwadza pano kudzatikuta. Ine ndaima pano kuti ndiyankhule m'malo mwa anamalira onse akuchikazi komanso akuchimuna Poyamba ndithokoze nonse posiya ntchito zanu kudzatikuta ife pa nthawi yowawitsa ndi yosaiwalikayi, Tidziwa mwasiya ntchito zanu podziwa kuti maliro nkulirana ife sitikadatha kuchita zonse tokha. Kachiwiri ndifotokoze matenda omwe awatenga malemu agona apawa.

Malemuwa adagwa pomwe amati alowe m'nyumba mwawo dzana. Mosazengereza tidatipa nawo Kuchipatala ku Chitalo komwe atawapima anawapeza ndi malungo aakulu. Mankhwala adalandira koma m'banda kucha wadzulo tidangoona akutilawira mosakhalitsa kupita kudali komweko dandaulo lanthu ndi ana, adzukulu ndi mferekazi omwe malemuwa asiya. Zateremu mtengo wakachere wagwa.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa**

a. Ndani adapita kukauza amfumu kuti mudzi watha kumanda?

_______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

b. Tchulani dzina la chipatala komwe wotisiyayu adatengeredwa?

_______________________________________________________________

_______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

**continued/….**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

c. Nchiyani chidachitika mfumu itaona kutha kwa mudzi?

_______________________________________________

(malikisi 2)

d. Kodi wotsogolera mwambo adayamba ndi chiyani m'malonje mwake?

_______________________________________________

_______________________________________________

(malikisi 2)

e. Nchiyani chomwe anthu adapephedwa kuti awonetse ulemu pa mwambo wa maliro?

_______________________________________________

_______________________________________________

(malikisi 2)

f. Kodi anthu oyakhula pamwambo wa maliro adapemphedwa kuchita chiyani kuti asunge nthawi?

_______________________________________________

_______________________________________________

g. Pezani mawu n'nkhaniyi omwe akufanana matanthauzo ndi mawu awa:

i. manda ________________________________ (malikisi 1)

ii. namfedwa ________________________________ (malikisi 1)

iii. yeza ________________________________ (malisiki 1)

h. Kodi omwalirayu amadwala chiyani?

_______________________________________________

_______________________________________________

(malikisi 1)

i. Perekani matathauzo a mikuluwiko iyi:

i. mtengo wakachere wagwa

_______________________________________________

(malikisi 2)

ii. tiugwire mtima

_______________________________________________

(malikisi 2)

j. Ndi dandaulo lanji lomwe oyimira anamalira adapereka kaamba ka imfa ya malemuwo?

_______________________________________________

_______________________________________________

(malikisi 2)

continued/….

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

EXAMINATION NO.:______________________

## Gawo C: (Malikisi 10)

**4.** Werengani kankhani ndipo muyankhe mafunso otsatirawa ndipo muyankhe mafunso otsatirawa.

' Zikomo Makolo nonse chifukwa chofika mwachikhadzakhadza motere. Nkhani yaikulu ndi yokudziwitsani za chitukuko chomwe talandira pano komanso dongosolo la kaphikidwe ka phala.

**Mafunso**

a. Ndi malonje anji aperekedwawa?

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

b. Kodi malonjewa angaperekedwe kuti?

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

c. Mawu oti "Chikhadzakhadza" akutanthauzanji?

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

d. Kodi getsi lachikasu pamsewu limatanthauza chiyani?

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

e. Perekani njira imodzi yosungira chikhalidwe cha Makolo

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

**5. KUPANGA ZIGANIZO**

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. tawo

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

b. osati

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

c. gada

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

d. memeza

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

e. madzulo

______________________________________________________________

**(malikisi 1)**

**continued/....**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C, kapena D) m'mafunso otsatirawa**

**6.** Tabiya si mlerankhungwa.
A. Muonjezi C. Mfotokozi
B. Mneni D. Mlomammalo

**7.** Kugona kofunika pa moyo wamuthu.
A. Mneni C. Dzina
B. Mvekero D. Muonjezi

**8.** Zonse zolowa m'khola.
A. Mlowammalo C. Mfotokozi
B. Mlumikizi D. Mneni

**9.** Achapa zovala za amayi.
A. Mlumikizi C. Mlowammalo
B. Mvekero D. Mperekezi

**10.** Alendowo adafika usiku.
A. Dzina C. Muonjezi
B. Mfotokozi D. Mneni

**Mafunso 11 mpaka 15: Sankhani mikuluwiko yotsutsana m'matanthauzo ndi mkuluwiko yotsatirayi.**

**11.** Ukayendera mzengo usamati asakhwi afumbula.
A. Ichi nchiyani nkulinga muli awiri.
B. Zengerezi adalinda kwawukwawu.
C. Ukayenda m'tchire wayendera zonse.
D. Pakadafunda padajiwitsa galu.

**12.** Mwala wogubuduzika suyanga ndere.
A. Chala chimodzi sichiswa nsabwe.
B. Choka m'mbuyo khwangwala atole mphutsi.
C. Tsiku limodzi siliwoza mbewa.
D. Pamodzi pamodzi padawoletsa dzungu.

**13.** Tsabola wakale sawawa.
A. Mawu aakulu akoma akagonera.
B. Lende nkukankhana.
C. Muyang'ana dzuwa adasokera.
D. Fumbi ndiwe mwini.

**14.** Wokaona Nyanja adakaona ndi mvuwu zomwe.
A. Phungu sataya nthenga.
B. Ukayendera mzengo usamati asakhwi afumbula.
C. Chilimwe ndipatse munda.
D. Sikadza kokha kuopa kulaula.

**15.** Mwana wa mzako ndi wako yemwe, ukachenjera manja udya naye.
A. Taleka ntalawa adatha mphika.
B. Mwana wang'ona sakuliraa dziwe limodzi.
C. Mwana wamwini ndi gaga saundika.
D. Tsiku limodzi siliwoza mbewa.

**Mafunso 16 mpaka 20: Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera zam'kalembedwe.**

**16.** A. Ana anati, "Timakonda kusambira."
B. Ana anati timakonda kusambira.
C. Ana anati, Timakonda kusambira.
D. Ana anati Timakonda kusambira.

**17.** A. Iwo; akufuna kukagula zinthu izi: mpunga, nsinjiro ndi mbatata.
B. Iwo akufuna kukagula zinthu izi: mpunga, nsinjiro ndi mbatata.
C. Iwo akufuna kukagula zinthu izi; mpunga, nsinjiro ndi mbatata.
D. Iwo akufuna kukagula zinthu izi: Mpunga, Nsinjiro ndi Mbatata.

**18.** A. M'mudzi mwathu mulibe mitengo
B. M' mudzi mwathu mulibe Mitengo.
C. Mmudzi mwathu mulibe mitengo.
D. M'mudzi mwathu mulibe mitengo.

**continued/....**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**19.**A. Kodi mwadya!
B. Kodi mwadya?
C. Kodi? mwadya.
D. Kodi, Mwadya.

**20.**A. Melifa namwino watisiya.
B. melifa, namwino, watisiya.
C. Melifa, namwino, watisiya.
D. Melifa, namwino, watisiya.

**Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani mawu ofanana m'matanthauzo ndi mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

**21.**Nasibeko waphika bota.
A. Thobwa C. Mbatata
B. Mowa D. Mpunga

**22.**Alendowa adakhala pa chikumba.
A. Mpando C. Chikopa
B. Thabwa D. Mkaka

**23.**M'munda mwa a Bwatani muli chambu.
A. Nyemba C. Fodya
B. Njoka D. Chiwindo

**24.**Nthumbali muli chipala chambiri.
A. Chimanga C. Gaga
B. Phulusa D. Nyemba

**25.**Chaka chino kuli mpupuluzi
A. Chinyezi
B. Masika
C. Usiwa
D. Njala

**Mafunso 26 mpaka 30: Sankhani misintho ya aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**

**26.**Mayi Nasibeko abzala chinagwa.

A. Wom'chitira
B. Wochitiridwa
C. Wotsutsa
D. Wochitisa

**27.**Agogo awaphikira chakudya.

A. Wom'chitira
B. Wochitirana
C. Wochititsa
D. Wonyazitsa

**28.**Botolo langa lasweka
A. Wochitirana
B. Wochitidwa poyera
C. Wochitidwa mchibisira
D. Wobwereza bwereza

**29.**Namwali wamwano wamenywa koopsa.
A. Wochitidwa
B. Wochititsitsa
C. Wochititsa
D. Wonyadzitsa

**30.**Iwo akambirana nkhani zosiyanasiyana.
A. Wobwerezebwereza
B. Wom'chitira
C. Wochitirana
D. Wotsutsa

Mafunso 31 mpaka 35. Sankhani mitundu ya afotokozi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

**31.**Galu wachiwewe waluma mwana.
A. Wamgwirizano
B. Waumwini
C. Wamaonekedwe
D. Wamakhalidwe

**32.**Mbuzi zisanu zagwidwa ndi galimoto.
A. Wopatula
B. Wamawerengero
C. Wochulukitsa
D. Waumwini

**33.**Buluku lobiriwira lasowa.
A. Wamaonekedwe
B. Woloza
C. Wamakhalidwe
D. Wamgwirizano

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

continued/….

**34.** Ophunzira yemwe salemekeza aphunzitsi sakondedwa.

A. Woloza
B. Wamakhalidwe
C. Wamgwirizano
D. Wochuluka

**35.** Sukulu yathu ndi yokongola.

A. Wofunsa
B. Waumwini
C. Wamaonekedwe
D. Waumwini

**Mafunso 36 mpaka 39: Sankhani ntchito za mayina omwe omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo**

**36.** Zondiwe bwera kuno.

A. La mwinimwini
B. La mwini chinthu
C. Loitanira
D. La malo

**37.** Kusukulu kwathu kulibe madzi.

A La malo
B. La ubale
C. Loitanira
D. Mwininkhani

**38.** Monika watenga kalata.

A. Mwininkhani
B. Pamtherankhani
C. Loitanira
D. La malo

**39.** Iye ndi katswiri.

A. La malo
B. Mtsirizi wa mneni
C. Loitanira
D. Lapadera

**Mafunso 40 mpaka 42: Sankhani nthawi za aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo**

**40.** Iye wadya mbatata.

A. Yakale yathayi
B. Yatsopano
C. Ya mtsogolo
D. Yamtsogolo yathayi

**41.** Chikondi azidzakhala kuno.

A. Yamtsogolo yopitirira
B. Yatsopano
C. Yamtsogolo
D. yatsopano yangothayi

**42.** Ndidyabe ndikamva njala.

A. Yamtsogolo yathayi
B. Yatsopano
C. Yamtsogolo
D. Yamtsogolo yopitirira

**Mafunso 43 mpaka 45: Sankhani nthambi za ziganizo zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**

**43.** Sadanene kumene wapita.

A. Yamfotokozi
B. Yamuonjezi
C. Yadzina
D. Yoima payokha

**44.** Adzabwera pokhapokha mudzamuyitane.

A. Yoima payokha
B. Yadzina
C. Yamfotokozi
D. Yamuonjezi

**45.** Iwo adya mango omwe ndidagula dzana.

A. Yamfotokozi
B. Yamuonjezi
C. Yoima payokha
D. Yadzina

# MAFUNSO ATHERA PANO

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com